Kalata ya No. 33

# UTHENGA WABWINO WA CHOONADI

Malangizo ndi Chilimbikitso kuchokera m'Baibulo kupita kwa amene akulalikira Uthenga Wabwino

## KUPATULIDWA KU UTUMIKI

Kupatulidwa kwa atumiki a Mulungu unali mwambo umene unkachitika mu mpingo woyamba ndipo uchokera mu Baibulo ndipo tikuyenera kutsatira chitsanzo chake ndi malangizo ake monga analembera mu Chipangano Chatsopano. Kupatulidwa mu mbiri yonse ya mpingo kwakhala kukuchitika koma mwandale nthawi zina—ndipo kwapotozedwa ndi kusokonezedwa; komabe izi sizitanthauza kuti mpingo usiye chiphunzitso ichi choona komanso kuchita mwambo uwu wa kupatulidwa kwa atumiki a Mulungu.

### Kodi kupatulidwa ndi chiyani?

Atumiki, ogwira ntchito ya Ambuye, adzisankhidwa ndi Ambuye ndipo akuyenera kuti adzozedwe ndi mphamvu komanso ulamuliro. Kupatulidwa ndiko kuvomereza pamaso pa gulu, molingana ndi Baibulo munthu amene Mzimu Woyera wamusankha ndi kumuyenereza. Zimenezi zimachitika pamaso pa gulu ndipo atumiki ena a Mulungu amene anapatulidwa kale amasanjika panja pa munthuyo. Malingana ndi buku la *Thayer's Greek Definitions*, kupatula ndiko "kuika, kupereka, kuika chinthu china pamwamba pa chinzake, kusankha wina kuti ayendetse ntchito, kuikiza, kukhazikitsa, kulengeza."

Tikabwera ku mpingo, kupatulidwa kumatanthauza kapena kumalengeza za kusankhidwa kapena kuitanidwa kwa munthu ku utumiki mu mpingo pamene aikidwa manja ndi atsogoleri ena ampingo amene anapatulidwa kale. Ndi mwambo wotsimikiza, umene Malemba amauvomereza pofuna kuti tionetse kuti tikuzindikira kuti mtumikiyo anaitanidwadi ndipo ali ndi zomuyenereza.

Paulo analembera kwa Tito kuti, "Chifukwa cha ichi ndinakusiya iwe m'Krete, kuti ukalongosole zosowa, nukaike akulu m'midzi yonse, monga ndinakulamulira" (Tito 1:5). Tito anatsalira ku Krete kuti apitirize ntchito imene anaiyamba Paulo ndikuti akamalizitse komanso anamuuza kuti "ukalongosole zosowa." Ntchito ya kupatula akulu sichinali chinthu chimene chinali chachilendo kwa Ayuda, popeza akulu a ma sunagoge achiyuda nawonso amapatulidwa.

Paulo anauza Timoteo kuti "ukoleze mphatso ya Mulungu, ili mwa iwe mwa kuika kwa manja anga" (2 Timoteo 1:6). Pali zitsanzo zingapo zimene zikuonetsa kuti kupatulidwa ndiko kusankhidwa kuchokera kumwamba kwa atumiki amene mpingo wawavomereza mwa Mzimu Woyera powapatula ndi kuwadzoza ku utumiki wao.

Ngakhale kuti sakukamba za kupatulidwa monga timakudziwira, talingalirani ndime ya pa Machitidwe 13:2-4 pamene akuti: "Ndipo pa kutumikira Ambuye iwowa, ndi kusala chakudya, Mzimu Woyera anati, "Mundipatulire Ine Barnaba ndi Saulo ku ntchito imene ndinawaitanirako. Pamenepo, m'mene adasala chakudya ndi kupemphera ndi kuika manja pa iwo, anawatumiza amuke. Pamenepo iwo, otumidwa ndi Mzimu Woyera..." Ndi Mzimu Woyera amene amapereka mphatso, amaitana, amayenereza ndiponso amatuma atumiki a Mulungu. Komabe pamakhala mwambo wowadzoza ndi kuwasindikiza umene tinganene kuti ndiwo wa kupatulidwa.

Kupatulidwa kuli koposa kupatsidwa kapepala ndi utsogoleri wa Mpingo. Pali chinthu chofunikira chokhudzana ndi kupatulidwa, monga momwe ubatizo uli ndi tanthauzo lalikulu kusiyana ndi nthawi imodzi imene munthu wamizidwa m'madzi.



"Pemphero lalikulu limene linalembedwa limadziwika kuti "Pemphero la Ambuye" ndipo ndi ndondomeko ya pemphero yakuti titsatire."


Kupatulidwa ku utumiki 1
Ndondomeko imodzi ya utumiki 2
Mau a Mkonzi 3
Cholinga ndi phindu la kupatulidwa 4-5
Zoyenereza malingana ndi Baibulo 5
Woyembekeza kupatulidwa 6
Ndondomeko ndi machitidwe ake 7
Kodi mukudziwa? Mau a nyengo yake Kodi kupatulidwa kumakhalapo mpakana liti? 8

# ZIMENE BAIBULO LIMAPHUNZITSA ZA...

**Mau a Mulungu**
2 Tim. 3:16-17; 2 Pet. 1:20-21; Mat. 24:35

**Ubale wa Chikondi**
Mat. 22:37-40; Yoh. 14:21-23; 1 Yoh. 4:7-11

**Kulapa**
Mach. 3:19; Mach. 17:30; 2 Akor. 7:10

**Kubadwa mwatsopano**
Yoh. 3:3-7; 2 Akor. 5:17; Aro. 6:1-4; Aef. 2:1, 5-6

**Kupulumuka ku uchimo**
1 Yoh. 5:18; Mat. 1:21; Yoh. 8:11

**Chidzalo cha Mzimu Woyera**
Mach. 19:2; Mach. 15:8-9; Mach. 1:8

**Chiyero**
Luk. 1:73-75; Aheb. 12:14; 1 Pet. 1:15-16; Tit. 2:11-12; Aro. 6:22

**Ufumu wa Mulungu**
Luk. 17:20-21; Aro. 14:17; Yoh. 18:36

**Mpingo**
Mach. 2:47; Aef. 4:4-6; 1 Akor. 12:12-13; Akol. 1:18

**Umodzi**
Yoh. 17:20-23; Agal. 3:28; Chiv. 18:2-4

**Maskaramenti**
Mat. 28:19-20; Mat. 26:26-30; 1 Akor. 11:23-27; Yoh. 13:14-17

**Machiritso**
Luk. 4:18; Yes. 53:4-5; Yak. 5:13-16

**Chiyero cha Banja**
Mat. 19:5-6; Luk. 16:18; Aro. 7:2-3; 1 Akor. 7:10-11

**Chikhalidwe cha pakati pa anthu ena**
1 Tim. 2:9-10; 1 Akor. 11:14-15; Deut. 22:5

**Masiku omaliza**
2 Pet. 3:7-12; Yoh. 5:28-29; 2 Akor. 5:10; Mat. 25:31-46

**Kukhala mwa mtendere**
Luk. 6:27-29; Luk. 18:20

**Kupembedza**
Yoh. 4:23-24; Aef. 5:19; 2 Akor. 3:17

**Kulalikira Uthenga Wabwino**
Mrk. 16:15

## NDONDOMEKO IMODZI YA UTUMIKI

Mu Malemba, pali kupatulidwa kwa akuluampingo ndi kupatulidwa kwa atumiki. Pamene mtumiki wa Mulungu wapatulidwa, Iye amapatulidwa monga mkuluwampingo. Mu mpingo woyamba, ngakhale kuti panali mphatso ndi maudindo osiyanasiyana komanso panali iwo amene amatumikira pa mpingo umodzi ndi ena otumikira m'madera okulirapo, komatu panali ndondomeko imodzi ya atumiki. Mau akuti mkuluwampingo ndi mau amene mulinso mau akuti bishopu, mkulu, woyang'anira ndi ena ndipo nthawi zina m'Malemba amagwiritsidwa ntchito mosinthanasinthana. Pa Tito 1:5 akugwiritsa ntchito mau a mkulu (*presbuteros*=akuluampingo) ndipo akupitiriza kupereka zomuyenereza munthuyo ndipo pa vesi 7 akugwiritsa ntchito mau akuti bishopu (*episkopos*=oyang'anira). Ndi udindo umodzi womwewo koma unangodetsedwa chifukwa cha chiphunzitso cha mpatuko chimene chinabwera m'zaka zotsatira. Pa mutu umenewu, wolembera uja Adam Clarke ananena kuti: "Kukuoneka kuti iwo amene akutchulidwa kuti akuluampingo pankhaniyi ndi omwewonso amene akuwagwiritsa ntchito pamene akunena za woyang'anira mu Tito 1:7. Tili ndi zitsimikizo zambiri zakuti mabishopu ndiponso akulu anali mu ndondomeko imodzi yomweyo mu mpingo wa atumwi, ngakhale kuti nkupita kwa nthawi udindo uliwonse ntchito yake inaonekera."

Kupatulidwa ndi mwambo wopereka udindo kwa munthu kukhala mkulu, OSATI ku ntchito ina ya utumiki wina mu mpingo, monga mbusa, wamishoni kapena mlaliki. Mkulu amene wapatulidwa mu utumiki wa uneneri ndi iye amene "waikidwa, ndi mpingo ngati ali ndi zomuyenereza ku umunthu, m'maganizidwe kapena ku uzimu kuti akhoza kutenga malo a wolalikira mu mpingomo" (*The Apostolic Church*, Charles E. Brown, 1947, p151).

Pamene chiphunzitso champatuko chinalowa ndi kukula kufika pa chikatolika, mphamvu ya utumiki inakula mwachangu kwambiri ndipo munthu anatenga udindo umene Mzimu Woyera amafuna kuti atenge m'miyoyo ya anthu. Pamene zaka zochuluka zinayamba kupita, panayamba kukhala mautsogoleri wokhala ndi malevulo osiyanasiyana zimene panalibe mu mpingo woyamba uja.

Malemba amatiphunzitsa kuti ulamuliro wa mpingo uli pa mapewa a Khristu, komanso amatiphunzitsa kuti anthu amalamulira motsogozedwa ndi Mzimu Woyera kudzera mu kuperekedwa kwa mphatso za uzimu. Nkofunika kuti mtumiki wa Mulungu aliyense amene amanena kuti amatsogoleredwa ndi mphatso za Mzimu Woyera adzipimidwa ndi atumiki ena amene ali odzazidwa ndi Mzimu Woyera molingana ndi m'mene iye akugwiritsira ntchito mphatso yakeyo. "Ndipo mizimu ya aneneri imvera aneneri" (1 Akorinto 14:32). Zimenezi sizikwaniritsidwa pokhala ndi atumiki amene anapatulidwa nakhala ndi maudindo osiyanasiyana koma kudzera mwa anthu a Mulungu amene agwirira ntchito limodzi ndiponso modzichepetsa koma akutsogozedwa ndi Mzimu Woyera.

*Gospel Truth* ndi kalata imene imasindikizidwa miyezi itatu iliyonse ndi a mpingo wa Church of God pofuna kulangiza ndi kulimbikitsa kuchokera mu zoonadi zopezeka mu Baibulo. Kuti mudziwe zambiri werengani pa intaneti popita pa www.thegospeltruth.org ndipo muvomere pa email imene mulandire ngati mukufuna kuti mudzilandira nawo kalatayi. Kalata ya *Gospel Truth* imasindikizidwa mu maiko ambiri kuti iperekedwe kwaulere m'dzikomo ndipo chuma chothandizira ntchitoyi chimachokera ku ndalama zimene ena amapereka mwaufulu. Ngati mukufuna lisiti yoonetsa zimene mwapereka, tidzakupatsani. —Editor, Michael Smith

Gospel Truth, P.O. Box 2042, Nixa, MO 65714 USA
editor@thegospeltruth.org

# Mau a Mkonzi



*Ndipo iwo adzaitana bwanji pa Iye amene sanamkhulupirira? Ndipo adzakhulupirira bwanji Iye amene sanamva za Iye? Ndipo adzamva bwanji wopanda wolalikira? Ndipo adzalalikira bwanji, ngati satumidwa? Monganso kwalembedwa, Okometsetsa ndithu ali mapazi a iwo akulalikira Uthenga Wabwino wa zinthu zabwino.!*—Aroma 10:14-15

Ndikunyadira kwambiri chifukwa cha iwo amene anaitaidwa ndi Mulungu ndipo analalikira mokhulupirika uthenga wabwino ndi waulemerero wa Yesu Khristu. Ndi Mzimu Woyera amene amaitana anthu ku utumiki. Mutu wathu ulendo ndi wa Kupatulidwa kwa atumiki a Mulungu. Ngati Ambuye alole, tidzakamba za kupatulidwa kwa madikoni mu kalata ikubwerayo. Tsoka ndilo, mau akuti 'kupatulidwa' amamveka mosakoma mkamwa mwa anthu ena chifukwa cha kusamvetsetsa, kuwagwiritsa ntchito molakwika, zopweteka komanso kuwasokoneza kumene kumachitika ndi iwo amene akulamulira mumpingo. Pemphero langa ndilo lakuti anthu pamene anthu akumvetsetsa, kupatulidwa kudzaoneka kuti ndi chinthu chabwino ku mpingo monga m'mene chilili.

Kupatulidwa ndi koposa kungolandira kapepala monga mwa lamulo. Kupatulidwa kuli umboni ndi chitsimikizo cha maitanidwe ndi kudzoza kwa Mulungu pa moyo wa mtumiki ku thupi la Khristu. Kuposa kwake ndi chiphunzitso chake zikuchokera m'mau a Mulungu ndipo chifukwa chaichi kumaposa zolingalira ndi maganizo a anthu. Kupatulidwa kuli chinthu chochitika ku uzimu chimene chili kudzipatula, kudzipereka, nthawi ya kulandira mdalitso ndi kukonderedwa kwapaderadera kuchokera kwa Mzimu Woyera pamene munthu amasanjikidwa manja ndi atumiki ena amene anapatulidwa kale.

Monga m'mene zimakhalira ndi ziphunzitso komanso zikhalidwe za Baibulo, nkofunika ndithu kuti timvetsetse bwino lomwe tanthauzo lakuuzimu la chinthuchi. Kupatulidwa kusakhale chinthu chongokhala ngati chikumbutso, kapenanso ngati zomwe zimachitika ndi zipembedzo zambiri, ndipo mu mpingo musakhale ndondomeko za maulamuliro molingana ndi udindo. Atumiki a Mulungu onse adzikhala ofanana mphamvu ndipo azidzodzedwa mu mautumiki awo, kaya ndi aang'ono kapena aakulu, opatulidwa kapenanso osapatulidwa. Komabe kumbali ina, kupatulidwa kuli ndi tanthauzo ndithu, nchifukwa chake zilipo nthawi zomwe atumiki amene anapatulidwa amakhala ndi ulamuliro wa Mulungu umene mtumiki wa Mulungu amene sanapatulidwe samakhala nawo. Mtumiki wa Mulungu amene wapatulidwa AKUYENERA mopanda choletsa chilichonse kukhala iye amene wayenerezedwa ndi kudzozedwa ndi Ambuye, ndipo akhale kuti anthu akumuchitira umboni.

Nkofunika kuti kupatulidwa kutengedwe mosamalitsa ndithu molingana ndi zoyenereza zochokera mu baibulo. Uzimu wa Kupatulidwa ukhoza kusuluka mu thupi la Khristu ngati anthu osayenera apatulidwa pongofuna kusangalatsa mtumikiyo kapena mpingo. Izi ndi m'mene ziliri m'maiko ambiri. Kupatulidwa si chinthu chandale chochitika pofuna kukondweretsana. Ambuye atithandize kuti mpingo wa Church of God usungebe chiyero cha kupatulidwa kwa atumiki a Mulungu.

Ngati mau apambali, pali malemba ena mu Chipangano Chatsopano amene amagwiritsa ntchito mau akuti 'kupatulidwa' (onani Machitidwe 1:22, 1 Timoteo 2:7, Machitidwe 14:23) koma sakunena za mwambo wakupatulidwa umene malemba ena amalemba. Ndakamba za Malemba amene amafotokoza za mwambo wa Kupatulidwa. Tiyeni tonse tikhale m'moyo wolemekeza ndi kukondweretsa Mulungu. Potsatira mau a m'bale Ostis Wilson, "Ngati tingakondweretse Mulungu, tidzakondweretsa wina aliyense amene akuyenera kukondweretsedwa."

Michael W. Smith

July 2020

Zambiri Zili pa
**INTANETI**

*Mukafuna kutipeza pa intaneti, mulembe www.thegospeltruth.org kuti mudzilandira makalata athu kapenanso kuti muone makalata akale.*

## Chobetchera

[*Bro. Ostis Wilson, ponena za pa Machitidwe 13:1-4 pamene Barnabasi ndi Saulo anapatulidwa kuti agwire ntchito.*]

"Ili linali lamulo lapadera ndi lomveka bwino kwa iwo ndipo anasala kudya ndi kupemphera asanalankhulidwe, ndipo anateronso ngakhale pamene Mzimu Woyera analankhula nawo. Iwo amafuna kutsimikiza ndithu kuti sakuphonyetsa. Ha! Taonani abale, kodi sitingalimbikitsidwe pa mfundo imeneyi ndi kulingalira za m'mene timachitira pa miyambo yathu ya kupatulidwa kuti ikhale yolemerera ndi yadongosolo kusiyana ndi m'mene timachitira nthawi zina. Ndikumva mkati mwanga kuti ndikhoza kutero."

CHOLINGA NDI PHINDU LA

# KUPATULIDWA

Pali zolinga zosiyanasiyana ndiponso zofunikira zokhudza kupatulidwa kwa atumiki a Mulungu mu mpingo wa Church of God. Phindu la zolinga zimenezi likuyenera kuyezedwa ndithu ndipo zisapeputsidwe chifukwa cha zofuna za munthu, kapena kaganizidwe kake kapenanso zimene sizimusangalatsa.



## Chitsimikizo cha chinachake chauzimu

Malingana ndi chiphunzitso cha Malemba, pali china chake chauzimu chimene chimaperekedwa pamene tikunena za kupatulidwa kwa mtumiki wa Mulungu. Paulo amakamba za kupatulidwa pamene anamulangiza Timoteo kuti: "Usanyalapsye mphatsoyo iri mwa iwe, yopatsidwa kwa iwe mwa chimenero, pamodzi ndi kuika kwa manja a akulu" (1 Timoteo 4:14). Phunziro la vesi imeneyl likunena zoonadi zake za mwambo ndi mchitidwe wa kupatulidwa.

Kupatulidwa ndi imodzi njira zingapo zofuna kutsimikizira utumiki wa munthu pakati pa anthu amene iye akuwatumikira.

***Usanyalapse mphatso imene ili mwa iwe.*** Mau akuti "mphatso" pamenepa akuchokera ku mau a chinenero cha Chigriki otchedwa, *char'-is-mah*—omwe tingawatanthauzire kuti cholowa chochokera kumwamba, cholandiridwa chauzimu, kuyenerezedwa pa chipembedzo kapenanso kukonderedwa. Thunthu la utumiki wonse wa Timoteo—kuitanidwa, kuyenerezedwa, udindo wake, mphatso ya Mulungu, komanso kupatulidwa kwenikweniko zonsezi zinali gawo limodzi la kukonderedwa ndi Mulungu. Timoteo samayenera kunyalapsa zimenezi. Paulo ananenanso za mphatsoyi pa 2 Timoteo 1:6. "Chifukwa chache ndikukumbutsa iwe ukoleze mphatso ya Mulungu, iri mwa iwe mwa kuika kwa manja anga." Paulo amalankhula kwa Timoteo monga tate kwa mwana wake pamene anati, "Khala okhulupirika ku mphatsoyo ndiponso ku ulamuliro umene wapatsidwa kuti uyang'anire." Utumiki wa Timoteo, maitanidwe ake ndi kuyenerezedwa kwake zonse zimene inali mphatso yochokera kwa Mulungu. Abale amene anazindikira maitanidwe ake ndi zomuyenereza zake anatsimikizira za mphatsoyo ndi kuyivomereza pa kuika manja pa iye pa nyengo ya kupatulidwa. Chifukwa cha ichi, kupatulidwako kunali 'gawo' la mphatso kapena cholowa chimene chinaperekedwa kwa Timoteo.

***Kusanjikidwa manja.*** Mphatso ya utumiki imene inaperekedwa ku gawo lina inaperekedwa ndi Mzimu Woyera kudzera mu kusanjikidwa manja monga anaonetsera Paulo ndi akulu ena a Mpingo. Palitu mwambo waukulu ndi wochokera m'Malemba wokhudza kusanjika manja. Pa Genesis 48:14, Israele anaika manja ake pa mitu ya Efraimu ndi Manase nawadalitsa iwo. Pa Numeri 27:18-20 Ambuye anamulangiza Mose kuti aike manja ake pa Yoswa pamaso pa wansembe ndi mpingo wonse wa anthu. Moseyo ndiye amene akulangiza Yoswa ndi kuika ulemerero wake pa Yoswa kuti potero Aisraele adzimumvera. Pa Duteronomo 34:9 akutsimikiza mfundo imeneyi: "Ndipo Yoswa mwana wa Nuni anadzala ndi mzimu wanzeru; popeza Mose adamuikira manja ake; ndi ana a Israele anamvera iye, nachita monga Yehova adauza Mose." Nkofunika kudziwa kuti pa nyengo zambiri, Mzimu Woyera anaperekedwa ku Mpingo woyamba pamene manja anaikidwa pa okhulupirira ndipo anapemphera. Mzimu Woyera anaperekedwa ndi Mulungu, koma panali mdalitso wapadera ndi mphamvu zimene zinaperekedwa kudzera mu pemphero logwirizana lopita kwa wopereka mphatsoyo. Pali mphamvu mu pemphero logwirizana ndiponso pamakhala kukonderedwa kwa Mulungu kumene mbali ina kumatakasidwa ndi kusanjika manja. Zimenezi zikuonetsa kuti "kusanjika manja" kumayendera limodzi ndi kupatulidwa kwa munthu ku utumiki.

***Ndi akulu (presbytery).*** Mau akuti *presbytery* akutanthauziridwa kuti akulu pa Luka 22:66 ndi pa Machitidwe 22:5. Kupatulidwa si kunali kochitika ndi mkulu mmodzi koma ndi gulu la akulu.

## Kuvomereza pamaso pa gulu za maitanidwe

Kupatulidwa ndi njira imodzi yotsimikizira utumiki wa munthu wina pakati pa iwo amene iyeyo akuwatumikira. Kumeneku ndi kuvomereza chimene Mulungu akuchita m'moyo wa munthu winawake ndipo ndi imodzi mwa njira zothandizira kuti anthu akhulupirire utumikiwo. Nkofunika kuti anthu adziwe ndi kumvetsetsa kuti munthu amene wapatulidwa amaimira chinachake chachikulu choposa iye mwini - chimene chili thupi la Khristu. Chimenechi ndiye chifukwa chimodzi chomwe kupatulidwa kudzitengedwa mosamalitsa osati mopepuka.

M'bale Ostis Wilson analemba motere mokhudzana ndi nkhaniyi: "Ndikukhulupirira kuti kuvomereza ndiko chinthu chimene chingawathandize atumiki a Mulungu amene iwo akutumikira nawo komanso amene adzatumikire pakati pawo. Komabe ndikuona kuti mwambo wa kupatulidwa umapyola pamenepo ndipo kusanjikidwa manja ndi anthu amene anadzazidwa ndi Mzimu Woyera kumaikiza chinachake chachilendo mwa munthu amene wasanjikidwa manja...Paulo akutsimikiza...kuti pali chinachake ndithu chimene chimaikizidwa kwa iwo pamene anasanjikidwa manja ndi anthu odzazidwa ndi Mzimu Woyera. Ndikuganiza kuti tikuyenera kuphunzitsa chimenechi kwa anthu athu makamaka kwa iwo amene akuyembekeza kupatulidwa ndi kuwakonzekeretsa kuti alandire chinachake chamtengo wapatali [kaya ndi mdalitso/kukonderedwa/kutsindikiza—awa ndi maganizo a mkonzi] kuchokera

kwa Mulungu pamene manja a atumiki odzazidwa ndi Mzimu Woyera aikidwa pa iwo."

## Kayendetsedwe ka Mpingo

Malemba amene tawanena kale mu Tito 1:5 akuti: "kuti ukalongosole zosowa, nukaike akuru m'midzi yonse." Ndime zotsatira mu buku la Tito zikupereka zinthu zowayenereza akulu kuti akhoza kupatulidwa. Mu ndime imeneyi, kupatulidwa kumakhala ndi tanthauzo lapaderadera. Chimodzi mwa zifukwa zimene kupatulidwa kumachitika kunali kufuna kukhazikitsa utsogoleri wovomerezeka ndi ulamuliro wauzimu mu mpingo. Pamakhala ndipo padzakhala mizimu yachilendo mu mpingo, ndipo nkofunika kudziwa kuti pali mtsogoleri wovomerezeka wauzimu amene anthu akhoza kumudalira kuti awalangize mu njira za chilungamo. Talingalirani zolemba zimene zinalembedwa kalekale za atumiki a Mulungu amu mpingo wa Church of God:

"Mipingo yoyamba imalamulidwa ndi atumwi m'masiku oyambirira enieni, koma kulamulira kumeneku sikuti kunali kwayuti mpaka munthu kupatulidwa. Kumangokhala kuonetsetsa kuti pali munthu mu mpingo amene ali wolemezeka ndi kudalirika amene akupereka chikoka pa zinthu zaumulungu, zokhudza makhalidwe abwino. Iwowanso anali auzimu amene anali kuyang'anira anthu m'zaka zosiyanasiyana za mpingo" (*The Apostolic Church*, Charles E. Brown, 1947, p123).

"Zoonadi, pali kayendetsedwa ka mpingo mu Church of God, ndipo amayendetsa ndi anthu.—anthu a Mulungu-amene anapatsidwa mphatso yapadera nagwirira limodzi ndi anthu enanso amene Mulungu anawapatsa mphatso, onsewo motsogozedwa ndi Mzimu Woyera" (*Church of Mulungu Doctrines*, Cecil Carver, 1979, p95).

"Nkoyenera ndithu kuti mtumiki aliyense akhoza kumva kumasuka pamene akugwira ntchito yake ya utumiki, ndipo akhoza kugwira bwino ntchito yake ngati akudziwa kuti akuvomerezedwa, akuthandizidwa, ndiponso ali ndi chitsimikizo cha atumiki ena a Mulungu komanso oyera mtima amene iye amatumikira pakati pawo. Kuti munthu akwaniritse bwino udindo wa kukhala 'Mkulu' kapena 'Oyang'anira' mu mpingo mu magawo onse, iye akuyenera kupatulidwa pa kusanjikidwa manja ndi atumiki ena amene anapatulidwa kale. Iye akhoza kulalikira ndiponso kudyetsa nkhosa popanda kupatulidwako, koma pamene tifika pa nkhani ya kulamulira komanso kulimbana ndi mavuto amene angabwere mu mpingo. Komabe iye adzagwira bwino ntchito ndipo adzalemekezedwa mu kuweruza kwake ngati utumiki wakewo uli wovomerezeka ndipo ena amauchitira umboni ndipo anthu amene akuwatumikirawo amadziwa za chimenechi" (*Faith and Victory*, Ostis Wilson, December 1979).

## Molingana ndi Lamulo

Kupatulidwa kotsimikizika, kwa lamulo ndiko kovomereza kuti munthuyo ali ndi zomuyenereza ndipo ali mtumiki yemwe analandiridwa mu chiyanjano cha mpingo. Maiko ndi mabungwe ena amafuna kuti zoterezi zichitike ngati atumiki akhoza kugwira ntchito zina za utumiki monga kukwatitsa maukwati, kukatumikira kundende ndi kuchipatala.

## Kuvomerezedwa kwa munthu

Utumiki umakhala kuti munthu akhale payekha, kaya ndi wopatulidwa kapena ayi. Ngakhale izi zili choncho, pali kulimbika mtima ndi chitonthozo zimene zikhoza kubwera chifukwa chakuti ukudziwa kuti atumiki anzako ali pambuyo pako ndipo akuvomereza chitsogozo ndi kudzoza kwa Mulungu pa moyo wako. Chimenechi si chifukwa cha kupatulira munthu, koma pali phindu pamenepa limene likhoza kuchepetsa mafunso, kaya ndi a mkati kapena a kunja kwa utumiki, maka ngati zonse zili bwino mu moyo ndi utumiki wake.



**Ngakhale patakhala kuti pali zolankhula zosiyanasiyana, zingakhale zothandiza kuti anthuwo adziwe zakuti pali mtsogoleri wauzimu wovomerezeka amene iwo akhoza kumukhulupirira kuti awalangize pa njira za chilungamo.**

## Zimene Baibulo linena za Zomuyenereza Woyang'anira Mpingo

1 Timoteo 3:1-7

Mauwa ali okhulupirika, ngati munthu akhumba udindo wa woyang'anira, aifuna ntchito yabwino.
Ndipo kuyenera woyang'anira akhale wopanda chirema, mwamuna wa mkazi mmodzi, wodzisunga, wodziletsa, wolongosoka, wokonda kuchereza alendo, wokhoza kuphunzitsa;
Wosati woledzera, kapena womenyana ndeu; komatu wofatsa, wopanda ndeu, wosakhumba chuma;
Woweruza bwino nyumba yache ya iye yekha, wakukhala nao ana ache omvera iye ndi kulemekezeka konse.
Koma ngati munthu sadziwa kuweruza nyumba ya iye yekha, adzasunga bwanji Mpingo wa Mulungu?
Asakhale wophunza, kuti podzitukumula ungamgwere mlandu wa mdierekezi.
Kuyeneranso kuti iwo akunja adzakhoza kumchitira umboni wabwino; kuti ungamgwere mtonzo, ndi msampha wa mdierekezi.

# Woyembekeza Kupatulidwa

## *WOYENERA KUPATULIDWA AKHALE WOTANI*

***Zomuyenereza.*** Mtumiki wa Mulungu amene akuyembekeza kupatulidwa akhale ndi kudzoza komanso maitanidwe ochokera kwa Mulungu pa moyo wake. Iye akwanitsenso zomuyenereza woyang'anira mpingo malingana ndi Malemba monga akunenera pa 1 Timoteo 3:1-7. Zomuyenereza izi molingana ndi Malemba zidziwike kwa amene amene akutumikira, komabe pasakhale chokayikitsa chilichonse m'moyo wa mtumiki wa Mulungu iyeyo asanapatulidwe. Mtumikiyo akuyenera kuimira thupi la Khristu ndipo akhale chitsanzo cha chiyero, chiphunzitso chabwino ndi mzimu wokhala ngati wa Khristu. Kudzodza kwa Ambuye kudzionekera kwa thupi lonse la Khristu, osati kwa ochepa chabe. Oyembekeza kupatulidwa akhale odalirika mu ntchito zao ndipo akhale aphindu ku utumiki kusiyana ndi kukhala osapindulitsa. Akhale angwiro mu magwiridwe awo a ntchito, kaya ndi yathupi kapena yauzimu, ndipo akhale opanda banga ndiponso akhale akuti anthu amawadalira ndi kuwachitira umboni. Ngakhale kuti kupatulidwa kuti maitanidwe aakulu, kusasokonezedwe ndi kuti iyeyo asalakwitse, popeza munthu aliyense amalakwitsa, amakhala ndi zofooka zake, komanso tizikhalidwe tina pa umunthu wake timene Mulungu amakhala kuti akutikonzabe.



"Mtumiki adzikhala woimira thupi la Khristu ndiponso wachitsanzo pa chiyero, wokhazikika mu chiphunzitso, ndi wokhala ngati Khristu mu mzimu mwake."

***Zotchinga.*** Poonjezera za zomuyenereza mtumiki zimene zatchulidwa kale, pali mndandanda uwu umene uli ndi zina mwa zinthu zimene zikhoza kuimitsa kaye kupatulidwa kwa mtumiki wa Mulungu: ngati zinthu kunyumba sizili bwino, ngati ali ndi mavuto obwerezabwereza, ngati anthu sakumukhulupirira kapena kumudalira, ngati ali wosakhulupirira pa kutumikira, ngati ulaliki wake uli wopanda nzeru ndi wosagwira mtima komanso ngati palibe kugwirira limodzi ndi mpingo wa Khristu.

***Nthawi yake.*** Mtumiki watsopano, posatengera zaka zake zakubadwa komanso chidziwitso chake, asapatulidwe mwansanga koma apatsidwe nthawi yakuti atsimikize utumiki wake mwa Ambuye, popeza pamakhala makhwekhwe auzimu amene mdaniyo watchera. M'bale Cecil Carver ananena kuti, "Mau amatiphunzitsa kuti mtumiki asapatulidwe mpakana ataonetsa kuti ndi woyeneradi. 'Asakhale wophunza' akutionetsa kuti tikuyenera kusamala kupatulidwa kusanachitike. Komanso mbali inayi, atumiki asachedwetse kwambiri kupatulidwa." (*Ziphunzitso za Church of God*, 1979).

Kupatulidwa si chinthu chimene tikuyenera kuchitengera mwachibwana ayi ndipo ndi chinthu chakuti tichione mwa umulungu onse. Paulo anapereka malangizo pa 1 Timoteo 5:22 kuti "Usafulumira kuika manja pa munthu ali yense, kapena usayanjana nazo zoipa za eni..." Ngati mkuluwampingo mwadala wapatula mtumiki wa Mulungu wosayenera, iyeyo ndiye kuti akutenga nawo gawo pa kusayenerako povomereza utumikiwo. Mtumiki wa Mulungu sakuyenera kugonjera ku zofuna za ena kuti apatule winawake ngati iyeyo sakuchimva komanso kulandira chitsimikizo kuchokera kwa Mzimu Woyera. Kupatula munthu wina kuti angokwaniritsa kugwira nthito inayake (monga kudalitsa ukwati ndi zina) sikwabwino molingana ndi kufunikira kwa kupatulidwa pokhapokha ngati zonse zomuyenereza munthuyo zili m'malo mwake.


Chenjezo limeneli likhozanso kugwiritsidwa ntchito pamene mtumiki wa Mulungu wachokera ku chiphunzitso china kapena mpingo wina. Ngakhale kudzoza kwa Mulungu kukuoneka kuti kulipo ndipo pali chivomerezo cha choonadi, pafunikabe nthawi kuti titsimikize ndithu za utumikiwo. Pa 1 Atesalonika 5:12 timawerenga kuti, "Koma, abale, tikupemphani, dziwani iwo akugwiritsa ntchito mwa inu." Zimatenga nthawi kudziwa chiphunzitso ndiponso moyo wake wa munthu, choncho sichanzeru kuthamangira kumupatula mtumiki wa Mulungu amene akufuna kuti mpingo wa Church of God umuvomereze.

***Zoyenera kulingalira.*** Malemba saika nthawi yokhazikika yakuti munthu akhoza kutumikira asanapatulidwe, chifukwa cha ichi, padzakhala kusiyana pakati pautumiki umodzi ndi unzake. M'bale Ed Wilson, mkuluwampingo mu mpingo wa Church of God, anaunikirapo zina zofunika kuzilingalira pa mutuwu. Ngati munthu wakhala akulalikira pa gome mosadukizadukiza kwa zaka 5 kufikira 7, ikhoza kukhala nthawi yabwino yolingalira za kupatulidwa kwake. Ikhoza kukhala nthawi ya kumupatula kapena kupereka chifukwa chimene sangapatulidwe, ndipo kukhoza kukhala kwabwino kwa iyeyo kuti afunse bwino lomwe ngati pali chomuletsa kuti asapatulidwe.

Ngati mtumiki wa Mulungu ali ndi chobetchera pa moyo wake, ayenera apitirize kupemphera, nafunefune Mulungu, ndipo kulimbikira mu Mzimu. Iye agwire limodzi ndi utumikiwo pofuna kuti anthu amukhulupirire komanso akhale wokonzeka kukonza zimene zikumuvuta pogwiritsa ntchito mau ndi zintchito. Chimakhala chinthu chopweteka kwa anthu kuti ayambe afumuka ku utumiki, komabe ngati kudzoza kapena maitanidwe a Mulungu palibe kapena sakuonedwa ndi atumiki ena odzazidwa ndi Mzimu Woyera, nthawi ngati izi kumakhala kwabwino kuwutula pansi utumikiwo pofuna kuti uthenga wabwino kapena anthu apindule. Kupatulidwa si chinthu chimene tidzichita kuchisakasaka. Komanso si "mapeto" kapena mlingo wa kupambana pa utumiki. Mtumiki sakuyenera kukakamiza kuti apatulidwe popeza paja "Mtulo wa munthu umtsegulira njira..." (Miyambo 18:16).

# Ndondomeko ndi machitidwe ake

## DONGOSOLO LA KUPATULIDWA



Malemba sanena za dongosolo lokhazikika lokhudza kupatulidwa. Iwo amapereka zomuyenereza munthu ndipo zina amazisiya m'manja mwa anthu a Mulungu otsogozedwa ndi Mzimu Woyera. Madongosolo ake amene alembedwa m'munsimu si malamulo ochokera mu Baibulo amene mtumiki aliyense akuyenera kuwatsatira, koma ndi zinthu zoyenera kuziganizira kuti zitimangirire pamene tikuyembekeza ndondomeko ya kupatulidwa. Monga anachitira mtumwi Paulo, inenso ndikulemba izi monga maganizo anga, osati ngati lamulo lochokera kwa Ambuye.

***Udindo.*** Udindo wopatula atumiki a Mulungu uli m'manja mwa abusa ndi akulu mu uzimu amene amaudziwa bwino moyo wa munthu wopatulidwayo. Aliyense amene akutsogolera mwambo wa kupatula mtumiki awafunse akulu angapo amene atumikira naye mtumikiyo ndipo aone ngati pali china chofanana chimene chili choletsa kapena chothandizira kupatulidwako. Nkutheka kuti mtumiki wa Mulungu sanapatulidwe chifukwa palibe amene anatenga udindo womuona mwina chifukwa chakuti kumene amatumikira ndikovuta kufikako. Zimenezi zisapangitse kuti anthu amuone mtumiki amene sanapatulidwe ngati wosayenera.

Atumiki a Mulungu asakakamizidwe kupatula munthu ngati sakutsimikizika ndi moyo wauzimu wa munthu amene akuganiziridwayo. Nkosavuta kuthana ndi nkhani imene ilipo kusiyana ndi kuti muyambe kuyikamba pamene zinthu zayamba kusakhala bwino. Nthawi yationetsa kuti nkofunika kwa atumiki ambiri kuti adekhe ndi kusamalitsa pamene zinthu zikuoneka kuti sizili bwino. Kupatulidwa ndi kwauzimu ndipo kusachitidwe mwandale kapena pongofuna kusangalatsana. Kuonjezera apo, pali udindo wina wosaonekera umene atumiki amene apatula munthu amakhala nawo pa iwo amene awapatula.

***Kufufuza.*** Chimakhala chinthu chanzeru kumufufuza mtumiki wa Mulungu asanapatulidwe. Mtumiki amene akugwira ntchito yopatula alankhule ndi uyo amene akuyembekeza kupatulidwa. Alankhule naye mozama zokhudza chiphunzitso kuti atsimikize kuti zonse zili tayale. Kungakhale kwabwino kukacheza ndi mkazi wake wa mtumikiyo kuti mutsimikize za kukhazikika kwake pa zinthu zauzimu ndipo mutsimikize ngati banjalo limamuchitira umboni iyeyo kukhala mtumiki wa Mulungu. Atumiki amene akupatula munthuyo alumikizane ndi mpingo umene mtumikiyo amatumikirako. Pakhoza kukhala mavuto ena obisika amene akhoza kuonekera ngati izi zitachitika. Nkwabwino kuthana ndi mavuto kupatulidwa kusanachitike kusiyana ndi kudzapanga cholakwika chimene simungathe kuchibweza.

Kupatulidwa ndi chinthu chimene chili ndi magawo awiri. Gawo loyamba ndilo lakuti utumikiwo umakhala kuti ukuvomereza ndi kuthandiza mtumikiyo. Ndipo gawo lachiwiri munthu wopatulidwayo amavomereza chimene mpingo wa Church of God uli pokhala thupi la Khristu. Kupatulidwa kwa anthu a mu kagulu kena kosiyana nafe pa chipembedzo ulibe phindu ndipo si ovomerezeka pakati pa mpingo wa Church of God.

Dongosolo ka kupatulidwa cholinga chake sikuti chilowerere madera onse komabe kumayenera kuchitike mosasiyako zina. Kusatengedwe ngati chiweruzo koma ngati chitsimikizo. Anthu amene akuyembekeza kupatulidwa osaope kapena kukana dongosololi.  Cholinga chake ndicho kubweretsa mdalitso wochokera kwa Mulungu ndi wa thupi la Khristu.

***Kusabisa zinthu.*** Chimakhala chaulemu kulumikizana ndi atumiki ena a Mulungu mu thupi la Khristu. Ngakhale kuti akulu awiri kapena atatu amene anapatulidwa kale akhoza kukhala ndi ulamuliro wopatula munthu molingana ndi Baibulo, chikhalidwe cha mwambo wa kupatulidwa chimatanthauza kuti mukuvomereza ndi kutsimikiza za utumikiwo. Nawonso mpingo ukuchita chimodzimodzi. Nthawi zambiri, kupatulidwa kochitika mobisa kapena pamene pali anthu ochepa sikufikira pa cholinga cha kupatulidwa. Dongosolo lake lidzichitika mwakuti kupatulidwa kudzioneka kuti ndi kovemerezeka ndiponso kosakayikitsa.

***Malo.*** Uli mdalitso kwa anthu a Mulungu ndiponso ndi umboni wakuti Mzimu Woyera akugwira ntchito pofuna kuchititsa mwambo wa kupatulidwa pamaso pa okhulupirira. Kuphatikiza apo, kuli kwabwino kupatula mtumiki pakati pa iwo amene iye akuwagwirira ntchito. Kupatulidwa kuli kuvomereza ndithu komanso kusangalalira zimene Mulungu akuchita ndi mtumikiyo komanso ngakhale kudzera mu moyo wake.

Kupatulidwa ndi chiphunzitso chochokera mu Baibulo chimene chikadali chofunikira pa m'mene Mpingo wa Mulungu walero umayendetsera ntchito yake. Kukuyenera kupatsidwa ulemu ndi kulemekezedwa. Akulu amene apatulidwa akuyenera kupatsidwa ulemu chifukwa cha ntchito zawo komanso ulamuliro wawo mwa Mzimu Woyera.

Paulo analemba pa 1 Timoteo 2:7 kuti, "umene anandiika ine mlaliki wake ndi mtumwi..." Ena mwa anthu olembera amamvetsetsa mau akuti 'kupatulidwa' pamenepa osati ngati kuvomereza za utumikiwo pa kusanjika manja, koma kuitanidwa ndi Mulungu kwa Paulo pa moyo wake. Ngakhale kuti kupatulidwa kwa munthu mu mpingo kuli ndi malo ake, chofunika kwambiri ndicho chakuti tonsefe tifunefune kupatulidwa kwenikweni kwa Yesu Khristu kupyolera mu kudzoza kwa Mzimu Woyera.

KODI MUKUDZIWA?


Pakati pa Ayuda, “Panthawi ya Kupatulidwa ya mkulu wa sunagoge, nthawi zonse panali akulu atatu amene amaika manja pa munthuyo. Potsatira izi, malamulo a mpingo woyamba amati pakuyenera kukhala ma Bishopu atatu panthawi imene Bishopu wina akupatulidwa” [*Jamieson-Fausset-Brown* ponena za pa 1 Timoteo 4:14].

Mau a Nyengo Yake

# KUFANANA MU UTUMIKI

*“Koma inu musatchedwa Rabi; pakuti Mphunzitsi wanu ali mmodzi, ndipo inu nonse muli abale. Ndipo inu musatchule wina atate wanu pansi pano, pakuti alipo mmodzi ndiye Atate wanu wa Kumwamba. Ndipo musatchedwa atsogoleri, pakuti alipo mmodzi Mtsogoleri wanu, ndiye Kristu. Koma wamkuru wopambana wa inu adzakhala mtumiki wanu. Ndipo amene ali yense akadzikuza yekha adzachepetsedwa; koma amene adzichepetsa mwini yekha adzakulitsidwa.* — Mateyu 23:8-12

Ngakhale kuti pali mphatso zosiyana, maitanidwe osiyana ndi machitidwe osiyana, pali kusasiyana pakati pa atumiki a Mulungu. Yesu anati, “ndipo inu nonse ndinu abale.” Iye amalankhula mwatchutchutchu motsutsana ndi maudindo komanso utumiki wokhala ndi maulamuliro osanjikizana. Ngakhale kuti tikuzindikira phindu la kupatulidwa ndiponso tikupereka mpata kuti anthu akhoza kugwiritsa ntchito ulamuliro wa uzimu umene umabwera chifukwa cha utumikiwo, pali kusasiyana pakati pa atumiki zimene zimachitika mu mpingo wa Church of God.



Yesu anaitana ophunzira ake nawauza kuti: “Ndipo Yesu anawaitana, nanena nao, Mudziwa kuti iwo amene ayesedwa ambuye a mitundu ya anthu amachita ufumu pa iwo; ndipo akulu ao amachita ulamuliro pa iwo. Koma mwa inu sikutero ai; koma amene ali yense afuna kukhala wamkulu mwa inu adzakhala mtumiki wanu; ndipo amene ali yense afuna kukhala woyamba mwa inu adzakhala kapolo wa onse.” (Marko 10:42-44).

“Ngakhale kuti mphatso zazikulu ndi zoyenereza zazikulu za atumwi ena zinawapangitsa iwo kukhala ofunikira kuposa anzawo ndipo anadzikundikira maudindo pa iwo eni, komabe panali muyezo wodzichepetsa ndi kusasiyana kwa utumiki kufikira nthawi imene chiphunzitso cha mpatuko inayamba” (*What the Bible Teaches*, F. G. Smith, 1914, p252).

Chiphunzitso ndi mchitidwe wa Kupatulidwa sutsutsana konse ndi choonadi chimenechi pamene atumiki a Mulungu amakhala akufunafuna kuti akhale ndi mtima ngati wa Khristu nadzitenga wokha monga wopanda ntchito (Afilipi 2:5-7) potsatira chitsanzo cha Ambuye.


Kuti Mutipeze

The Gospel Truth
P. O. Box 2042
Nixa, MO 65714
USA

Email:
editor@thegospeltruth.org


CHIYERO CHA KWA AMBUYE

### Kodi kupatulidwa kumakhalapo mpakana liti?

Kupatulidwa komanso ulamuliro wa uzimu wa mtumiki umakhalapobe pokhapokha ngati chiphunzitso ndi machitidwe ake zili molingana ndi Malemba. Kudziwa chimenecho ndi chinthu chabwino komanso chofunikira ngati iyeyo akupitirirabe kutumikira pansi pa kudzoza kwa Mzimu Woyera ndipo kuti abale amamukhulupirira ndi kumudalira.